**Lamulo lapadera kuchokera ku boma la Malawi pa 14 January, 2021**

**Muli Lamulo, Zofunika kutsata, ndi zina zotero. (No. 1A)**

CHIDZIWITSO CHOYAMBA KUCHOKERA KU BOMA LA MALAWI

LAMULO LOPEREKA KUTHEKERA KOPEZA UTHENGA

(NO. 13 OF 2017)

# LAMULO LOPEREKA KUTHEKERA KOPEZA UTHENGA, 2021

## NDONDOMEKO YA BUKHULI ILI MOTERE

LAMULO

GAWO 1—POYAMBA

1. Katchulidwe
2. Katanthauziridwe

GAWO 2_ADINDO OPEREKA UTHENGA, NTHAMBI ZA BOMA NDI KAPEREKEDWE KA UTHENGA

3. Kasankhidwe ka adindo opereka uthenga
4. Ntchito za adindo opereka uthenga
5. Kasungidwe ndi Kasamalidwe ka Uthenga
6. Kuika uthenga pa makina a Kompyuta
7. Kupereka/kusindikiza uthenga
8. Ma lipoti a pachaka ndi ndondomeko za ntchito

GAWO 3_MABUKU OTSOGOLERA NDI OPEREKERA UTHENGA

9. Kapezekedwe ka mabuku otsogolera
10. Kapezekedwe ba bukhu la uthenga

GAWO 4_KUPEMPHA NDI KUPEREKA UTHENGA

11. Pempho la uthenga
12. Pempho lodzera pa Kompyuta
13. Ndondomeko zotsatira pa pempho lofuna kupeza uthenga
14. Kuthekera kwa kapezedwe ka uthenga
15. Chidziwitso kwa anthu okhuzidwa
16. Ndondomeko ya kaperekedwe ka uthenga
17. Ndalama zoyenera kulipira
18. Mfundo zoyenera kutsata pa kagwiritsidwe ntchito ka uthenga omwe waperekedwa
19. Kaperekedwe ka uthenga ku dziko lonse
20. Kupititsa pempho ku nthambi ina ya boma
21. Uthenga omwe sungapezeke kapena omwe palibe
22. Kukanizidwa kupeza uthenga

GAWO 5__KAUNIUNI WA MKATI

23. Pempho loti chiganizo cha bungwe kapena nthambi ya boma yomwe kukupezeka uthenga chiunikidwe

24. Ndondomeko zoyenera kutsata powunika chidandaulo



LAMULO

GAWO 6__KUUNIKIDWA KWA CHIGANIZO CHA NTHAMBI YA BOMA NDI BUNGWE LA MALAWI HUMAN RIGHTS COMMISSION

25. Kuwunikidwa mwapadera kwa chiganizo cha bungwe kapena nthambi ya boma yomwe kukupezeka uthanga

26. Ufulu omveredwa

27. Kupereka chiganizo

GAWO 7__ZINA ZOONJEZERA

28. Kukanizidwa kuti uthenga uperekedwe

29. Kusagwiritsa bwino ntchito uthenga omwe waperekedwa

30. Ndondomeko ya kagawidwe ka ndalama zoyenera kugwiritsa ntchito

31. Ndondomeko zoyendetsera

NDONDOMEKO YOYAMBA- ZOYENERA KULIPIRA

NDONDOMEKO YACHIWIRI- MAFOMU

POGWIRITSA ntchito mphamvu zomwe zinaperekedwa mu gawo 55 ya Lamulo lopereka kuthekera kopeza Uthenga, Ine, GOSPEL KAZAKO, Nduna yofalitsa Nkhani ndapanga Malamulo otsatilawa_

GAWO 1_POYAMBA

Katchulidwe

1. Malamulo amenewa atha kutchulidwa kuti Malamulo Opereka Kuthekera Kopeza Uthenga, 2021.

Katanthauziridwe

2. M'malamulo amenewa, pokhapokha ngati pali katanthauziridwe kena "munthu ofuna uthenga" ndi yemwe wapereka pempho lofuna kupeza uthenga kuchokera ku bungwe kapena nthambi ya boma

GAWO 2_ADINDO OPEREKA UTHENGA, NTHAMBI YA BOMA NDI KUPEREKA UTHENGA

Kusankha adindo opereka uthenga

3.__(1) Mkulu wa bungwe kapena nthambi ya boma adzasankha munthu wa udindo waukulu kukhala oyang'anira kupereka uthenga.

(2) Mkulu wa bungwe kapena nthambi ya boma adzapereka dzina la m'dindo opereka uthenga kwa Anduna.

(3) Anduna adzasindikiza maina a adindo opereka uthenga mu manyuzipepala osachepera awiri omwe amafikira dziko lonse kumayambiriro kwa chaka cha ndondomeko ya chuma cha boma chili chonse.

(4) Ngakhale mu gawo laling'ono mayina asindikizidwa,bungwe kapena nthambi ya boma idzasindikiza maina ndi momwe anthu angalumikizirane ndi adindo opereka uthenga pa tsamba lake la intaneti.

(5) Bungwe kapena nthambi ya boma itha kukhala ndi adindo opereka uthenga opitilira m'modzi ndipo zikakhala choncho pazakhala malire a udindo ndi utsogoleri.

**Ntchito za adindo opereka uthenga**

4.__(1) M'dindo opereka uthenga azayenera kupanga izi__

(a) Kuonetsetsa kuti bungwe kapena nthambi ya boma yachitapo kanthu pa mapempho a uthenga m'nthawi yoyikika.

(b) Kuthandizira kupereka uthenga omwe bungwe kapena nthambi ili nawo oyenera kuperekedwa ngakhale usanapemphedwe;

(c) Kuthandizira kusintha uthenga pa tsamba la intaneti la nthambiyo;

(d) Kugwira ntchito limodzi ndi ofalitsa nkhani wa nthambiyo powonetsetsa kuti uthenga ukupezeka; ndi

(e) Kuwonetsetsa kuti uthenga omwe waperekedwa watsimikizidwa ndi mkulu wa bungwe kapena nthambiyo.

Kasungidwe ndi kasamalidwe ka mbiri

5.__(1) M'dindo opereka uthanga azaonetsetsa kuti bungwe kapena nthambi ya boma yasunga uthenga mosamala ndi mwandondomeko yosavuta kupeza.

(2) Bungwe kapena nthambi ya boma idzayenera kukhala ndi tsamba la intaneti lomwe lizidzasinthidwa pafupipafupi.

(3) Tsamba la intaneti la nthambiyo lidzakhala ndi zinthu zosachepera izi_

(a) Ntchito za nthambiyo;

(b) Maudindo ndi ntchito za nthambi ndi zambiri zokhuza adindo ofunikira;

(c) Dera, keyala ya pa intaneti za nthambiyo,ndi;

(d) Dzina ndi momwe anthu angalumikizirane ndi m'dindo opereka uthenga.

6. Bungwe kapena nthambi ya boma idzaika pa makina a Kompyuta uthenga omwe ili nawo monga momwe anduna ananenera.

7.__(1) Bungwe kapena nthambi ya boma idzaonetsetsa kuti gawo 15 la lamuloli lasindikizidwa pasanathe masiku 6 kuchokera pomwe linakhazikitsidwala.

(2) Bungwe kapena nthambi ya boma idzapanga bukhu lomwe lidzakhale ndi izi_

(a) Ntchito za nthambiyo; ndi

(b) Masomphenya ndi mfundo zikuluzikulu za nthambiyo.

(3) Bungwe kapena nthambi ya boma idzaika bukhuli pa tsamba lake la intaneti ndipo likazapemphedwa,lidzapereka kwa yemwe angapemphe uthenga

(4) Powonjezera zomwe zanenedwa mu gawo laling'ono(3) la malamulo,bungwe kapena nthambi ya boma ngati yawona kuti ndikofunikira kutero,idzasindikiza uthenga m'manyuzipepala ofikira dziko lonse,kufalitsa pa wailesi,wayilesi ya kanema ndi njira zina powonetsetsa kuti uthengawo wafikira anthu ambiri.

Kusindikiza uthenga

Kupereka uthenga

8.__M'dindo opereka uthenga, pakadzatsala miyezi itatu kuti chaka cha chuma cha boma chithe, adzalemba lipoti la momwe nthambiyo yagwirira ntchito m'chaka chomwe changotha ndi kulemba ndondomeko ya momwe agwirire ntchito m'chaka chotsatira.

Ma lipoti a pachaka ndi ndondomeko ya ntchito

GAWO 3—MABUKU OTSOGOLERA NDI KUPEREKA UTHENGA

Kupezeka kwa mabuku otsogolera

9.—(1) Bungwe la Malawi Human rights Commission lizasindikiza bukhu lotsogolera molingana ndi gawo 9 la lamulo mu Chingelezi ndi zilankhulo zina zome zimagwiritsidwa ntchito.

(2) Bungwe la Malawi Human Rights Commission litha kudzasindikizanso bukuli malingana ndi gawo laling'ono la lamulo muzilankhulo zina likadzaona kuti ndikofunikira kutero.

(3) Bungwe la Malawi Human Rights Commission lidzaonetsetsa kuti bukhu losindikizidwalo likupezeka kwa omwe angalifune—

(a) Kwa adindo opereka uthenga omwe ali mu nthambi za boma;

(b) Kuwerengedwa ndi anthu ku maofesi a bungwe la Malawi Human Rights Commission nthawi yogwira ntchito, ndi

(c) Pa tsamba la intaneti la Malawi Human Rights Commission.

(3) Bungwe la Malawi Human Rights Commission litha kuzalipiritsa ndalama potengera mtengo omwe walembedwa mu ndondomeko yoyamba yomwe yalembedwa ngati bukhuli laperekedwa m'njira osati yomwe yanenedwa mu gawo laling'ono (2) la lamulo.

(4) M'dindo opereka uthenga wa bungwe kapena nthambi ya boma, asanathe masiku 30 ogwira ntchito atalandira bukhu lotsogolera kuchokera ku Malawi Human Rights Commission malingana ndi gawo laling'ono (2)la lamulo,adzaonetsetsa kuti aliyense ogwira ntchito ku bungwe kapena nthambi ya boma ali ndi mwayi okhala kapena kugwiritsa ntchito bukhuli.

(5) M'dindo opereka uthenga—

(a) Nthawi yogwira ntchito, akapemphedwa adzapereke mwayi kuti anthu athe kuliona bukhulo;

(b) Sazalipiritsa kuti anthu athe kuliona bukhulo malingana ndi gawo(a); ndi

(c) Ngati bukhu kapena gawo la bukhu litapezeka kapena kuperekedwa mu njira ina osati yomwe yanenedwa mu gawo(a), atha kulipiritsa mtengo omwe walembedwa mu ndondomeko yoyamba.

Kapezeked we ka mabuku

10.—(1) Bungwe kapena nthambi ya boma,likasindikiza bukhu la uthenga potsatira gawo 16(1) la lamulo kapena zina zikaonjezeredwa kapena kuchotsedwa malingana ndi gawo 16(3),nthambi ya boma izaonetsetsa kuti bukhuli likupezeka nthawi yomweyo ku—

(a) Malawi Human Rights Commission;

(b) Ma ofesi a bungwe kapena nthambi ya boma kuti anthu athe kuwerenga nthawi yogwira ntchito; ndi

(c) Pa tsamba la intaneti la nthambiyo.

(2) Ngati bukhu lotsogolera laperekedwa kapena kugawidwa m'njira yomwe sinalembedwe mu gawo laling'ono (1),bungwe kapena nthambi ya boma itha kulipiritsa mtengo omwe walembedwa mu ndondomeko yoyamba.

Kupempha uthenga

## GAWO 4_KUPEMPHA NDI KUPEREKA UTHENGA

11.__(1) Kupempha uthenga kuzachitika pogwiritsa ntchito Fomu 1 yomwe ili mu gawo lachiwiri mu bukhuli.

(2) Bungwe kapena nthambi ya boma idzaonetsetse kuti fomu yomwe ili pa gawo la lamulo (1)ikupezeka pa kompyuta ndipo yaikidwa pa tsamba la intaneti la nthambiyo.

(3) Fomu yomwe ikukambidwa mu gawo (1) la Lalamulo, itha kupezeka ku bungwe kapena nthambi ya boma komwe pempho la uthenga laperekedwa.

(4) Pempho la uthenga lidzayenera kukhala ndi tsatanetsatane okwanira wa munthu yemwe akupempha uthenga ndi uthenga omwe akufuna kupeza kuti pempholo lichitike.

(5) Ngati pempho la uthenga lilibe tsatanetsatane okwanira la opempha uthenga kapena uthenga omwe akufuna, m'dindo opereka uthenga adzapempha ofuna uthenga kuti apereke zofunikirazo kuti pempholo lichitike.

(6) Ngati opempha uthenga walephera kupereka zofunika zomwe zinapemphedwa monga mwa lamulo la gawo laling'ono(5), m'dindo opereka uthenga adzayesetsa kuthandiza ofuna uthenga momwe angathere kuti apereke zofunika:

Pokhapokha ngati m'dindo opereka uthenga watsimikiza kuti ofuna uthenga watsimikiza kuti zomwe amafuna zapezeka ngakhale wachita kuthandizidwa

(7) Ngati ofuna uthenga wapereka chifukwa chokwanira kulephera kupempha uthenga kudzera pa fomu yoyenera kugwiritsa ntchito ndipo wapereka pempho podzera mukuyankhula, pempholo lidzalembedwa ndi m'dindo opereka uthenga pa fomu ndipo zolembedwazo zizawerengedwa kwa ofuna uthenga kuti atsimikize.

(8) M'dindo opereka uthenga sakuyenera kukana kupereka mwayi opeza uthenga pachifukwa chakuti pempho silinalembedwe pa fomu yoikika yopemphera uthenga

(9) Malingana ndi gawo laling'ono (7) la malamulo, zifukwa zokwanira ndi kusatha kulemba ndi kuwerenga, ulumali komanso ngati munthuyo ndi wam'ng'ono.

12.__(1) Ofuna uthenga atha kutumiza pempho kudzera pa makina a intaneti ovomerezeka la bungwe kapena nthambi yaboma komwe kukupezeka uthenga.

(2) Pempho lofuna uthenga likatumizidwa kudzera mu njira ya pa kompyuta, m'dindo opereka uthenga adzasindikiza ndi kulisunga pempholi m'mabuku a bungwelo.

(3) Bungwe kapena nthambi ya boma idzakhazikitsa ndondomeko yoyankha yokha ngati pempho lapemphedwa pogwiritsa ntchito makina a intaneti:

(4) M'dindo opereka uthenga adzayenera kuvomereza kuti walandira pempho kudzera pa intaneti pasanathe masiku asanu ogwira ntchito kuchokera tsiku lomwe walandira pempholo.

13.__(1) Bungwe kapena nthambi ya boma idzadziwitsa chiganizo chake chopereka uthenga kapena ayi kwa opempha uthenga mu fomu 2 ya ndondomeko yachiwiri pasanathe masiku khumi ndi asanu kuchokera tsiku lolandira pempho

(2) Bungwe kapena nthambi ya boma likavomera kupereka mwayi opeza uthenga, m'dindo opereka uthenga adzadziwitsa opempha uthenga pasanathe masiku asanu chipangireni chiganizocho__

Pempho kudzera pa intaneti

Ndondomeko ya kaperekedwe ka uthenga

(a)ofuna uthengawo awunike kaye uthenga usanasindikizidwe kupewa kugwiritsa ntchito ndalama zambiri pobwereza kusindikiza;

(b) kuti ofuna uthenga atha kunena ngati akufuna chabe magawo ena a uthenga kuti usindikizidwe;

(c) Za kuchuluka kwa ndalama zomwe zingafunike kuti alipire uthenga usanasindikizidwe kapena kukonzedwa kuti uperekedwe;

(d) Za mtengo onse pamodzi osindikiza ndi kukonza uthenga kuti uperekedwe; ndi

(e) Za mtengo oyenera kulipira uthenga usanaperekedwe kuphatikizirapo ndalama yosindikizira

(3) Ngati pakufunika kulongosola kowonjezera kuti uthenga omwe wapemphedwa upezeke, m'dindo opereka uthenga azadziwitsa ofuna uthenga pasanathe masiku asanu ndi awiri chilandilireni pemphoro kuti alongosole bwino.

Kupereka chilolezo kuti uthenga uperekedwe

14.__(1) Pempho lopeza uthenga likavomerezedwa, opempha uthengayo, asanathe masiku makumi atatu chidziwireni chiganizo cha bungwe kapena nthambi ya boma komanso pogwiritsa ntchito ma ola okhazikika ogwirira ntchito, ku ma ofesi.

(3) Wamkulu wa bungwe kapena nthambi ya boma adzaonetsetsa kulondola kwa uthenga operekedwa kwa opempha uthengayo.

Kupereka pempho ku nthambi zina

15.__(1) M'dindo opereka uthenga akalandira pempho lofuna uthenga okhudza munthu kapena nthambi ina ya boma, m'dindo opereka uthengayo azadziwitsa munthu kapena bungwe linalo pogwiritsa ntchito fomu 3 yomwe ili mu ndondomeko yachiwiri la pempho la ofuna uthenga.

(2) Bungwe kapena m'dindo wina okhudzidwa yemwe wapatsidwa chidziwitso malingana ndi lamulo la gawo (1) adzafunika kupereka yankho malingana ndi chidziwitsocho pasanathe masiku khumi ogwira ntchito kuchokera tsiku lomwe analandira pempho.

(3) Ngakhale ena okhudzidwa atanena kuti uthenga opemphedwawo siwoyenera kuperekedwa, koma ngati m'dindo opereka uthenga waona kuti uthengawo ndi oyenera kuperekedwa kwa anthu, m'dindo opereka uthengayo adzadziwitsa ena okhudzidwawo za chiganizo chake ndipo adzapereka uthenga kwa opempha uthenga.

Kaperekedwe ka uthenga

16.__(1) Ngati pempho la uthenga likufunika kuti fotokope iperekedwe, fotokopeyo idzaperekedwa m'njira yomwe yapemphedwayo.

(2) Posatengera lamulo laling'ono (1) pempho la uthenga litha kudzaperekedwa m'njira yosiyana ndi njira yomwe inapemphedwa ngati—

(a) Uthenga omwe uli ndi nthambi yomwe kuli uthenga usali mukapangwidwe komwe kapemphedwako; ndi

(b) Ngati bungwe la boma laona kuti pempho losintha uthenga kuti uperekedwe m'njira ina liri losayenera.

(3) Mfundo zotsatilazi zizagwiritsidwa ntchito popanga chiganizo ngati ndikoyenera kusintha uthenga kupita m'njira yomwe yapemphedwayo_

(a) Ngati pali kuthekera kowononga uthengawo pomwe ukusinthidwa;

(b) Ngati uthengawo ukupezeka ku bungwe la boma lomwe kuli uthenga mu kapangidwe komwe ofuna uthenga angathe kugwiritsa ntchito;

(c) Kuthekera kosintha uthenga omwe wapemphedwawo mukapangidwe kena komwe kangapangitse uthenga opemphedwawo kupezeka mosavuta;

(d) Zotsatira pa kagwiridwe ka ntchito za bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga chifukwa chosintha uthengawo;

(e) Kapezekedwe ka anthu ndi zipangizo zoyenera ku nthambi ya boma komwe kukupezeka uthenga oti asinthe uthenga kupita ku kapangidwe komwe kapemphedwa;

(f) Kupezeka, ku bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga, kwa luso loyenera ndi zipangizo zosinthira uthenga; ndi

(g) Mtengo, ku bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga, osinthira uthenga kupita mukapangidwe komwe kapemphedwa.

Ndalama zolipira

17.__(1) Ofuna uthenga sadzapereka ndalama iliyonse popereka pempho lofuna uthenga ku bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga.

(2) Ngati pempho la uthenga likupempha kuti uthengawo ukhale pawiri, kutanthauzira ndi kulemba, bungwe lomwe liri ndi uthengalo litha kupempha ofuna uthengayo kuti alipile malingana ndi mitengo yokhazikika yomwe yalembedwa mu ndondomeko yoyamba mu malamulowa.

(3) Ngati ofuna uthenga walipira ndalama yotulutsira uthengawo pawiri, yotanthauzira komanso kulemba, m'dindo opereka uthenga adzalemba ndi kupereka lisiti kwa ofuna uthenga.

Kagwiritsidwe ntchito ka uthenga

18.__(1) Ngati bungwe la boma liri ndi uthenga lipereka uthengawo kwa ofuna uthenga, bungwelo litha kuika mfundo zoyenera kutsata pakagwiritsidwe ntchito ka uthenga.

Kupereka uthenga ku dziko lonse

(2) Ngati uthengawo utadzagwiritsidwe ntchito mu chikalata, ofuna uthenga akuyenera pasanathe masiku asanu ogwira ntchito kuchokera tsiku lomwe asindikiza chikalatacho, kupereka fotokope ku bungwe la boma lomwe kunapezeka uthengawo.

19.__Ngati uthengawo utadzagwiritsidwe ntchito mu chikalata, ofuna uthenga akuyenera pasanathe masiku asanu ogwira ntchito kuchokera tsiku lomwe asindikiza chikalatacho, kupereka fotokope ku bungwe la boma lomwe kunapezeka uthengawo.

Kupititsa pempho ku nthambi ina

20.__(1) Ngati bungwe la boma lomwe kungapezeke uthenga laona kuti uthenga omwe wapemphedwawo ukupezeka ndi bungwe lina la boma, bungwe la boma lomwe liri ndi uthenga lomwe lalandira pempho, lizadziwitsa ofuna uthenga, pasanathe masiku asanu chilandilireni pempho, ndikusamutsa pempho kupita ku bungwe lina la boma lomwe liri ndi uthenga pogwiritsa ntchito fomu 4 yomwe ili mu ndondomeko yachiwiri

(2) Pempho lofuna uthenga likapititsidwa ku nthambi ina malingana ndi gawo (1) la malamulo, m'dindo opereka uthenga ku bungwe linalo komwe pempholo lapititsidwa azadziwitsa opempha uthenga kuti walandira pempholo ndipo akuliunika monga akanachitira pemphoro likanafikira kwa iye pachiyambi pomwe.

(3) Pempho lofuna uthenga likasamutsidwa kupita ku bungwe lina la boma lomwe kukupezeka uthenga, nthawi yochitapo kanthu pa pempholi idzayamba kuwerengetsedwa pomwe pempholo lasamutsidwa, kuchokera tsiku lomwe fomu 4 yalandiridwa ndi bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga.

Uthenga omwe sungapezeke kapena palibe

21.__(1) Pempho lofuna uthenga likakhala kuti likukhudza uthenga omwe__

(a) Waonongeka;

(b) Sungapezeke; kapena

(c) Uthengawo palibe,

m'dindo opereka uthenga adzalemba chidziwitso pasanathe masiku asanu chidziwireni kuti uthengawo supezeka, chodziwitsa ofuna uthenga, kuti uthengawo supezeka.

(2) Chidziwitso chomwe chalembedwa malingana ndi gawo laling'ono (1) la malamulo chidzakhala ndi umboni oyesera kufufuza uthengawo.

Kukanizid wa uthenga

22.__(1) Pomwe pempho lopempha uthenga lakanidwa, m'dindo opereka uthenga akuyenera kumudziwitsa ofuna uthenga pomulembera za chigamulochi kuphatikiza ndi zifukwa zake zomwe.

(2) Pamene mwayi opeza uthenga sunaperekedwe, ofuna uthengayo atha kusuma kwa mkulu wa bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga kuti aunikirenso chigamulochi malingana ndi lamulo 23.

Kuwunika kwa mkati

## GAWO 5_KUWUNIKA KWA MKATI

23.__(1) Ngati munthu sanakhutitsidwe ndi chigamulo cha bungwe kapena nthambi ya boma yomwe kukupezeka uthenga,odandaula atha kulembera kalata mkulu wa nthambiyo pogwiritsa ntchito fomu 5 yomwe ili mu ndondomeko yachiwiri,kuti chigamulo chiunikidwenso

(2) Malingana ndi gawo (1) la malamulo, munthu odandaula ndi__

(a) munthu ofuna uthenga yemwe__

(i) Sanapatsidwe mwayi opeza uthenga omwe anapempha:

(ii) Sanapatsidwe uthenga omwe anapempha m'nthawi yoikika ndiponso sanauzidwe zifukwa zomveka zomwe uthenga wachedwera; kapena

(iii) Sanakhutitsidwe ndi momwe pempho likuyendetsedwera, ndipo

(b) Munthu/bungwe wa/lapadera yemwe wafotokozeredwa mu gawo 35 la Lamulo, limene/amene zokhuza iye zaululidwa popanda chilolezo chake.

(3) M'dindo opereka uthenga azadziwitsa polemba, ofuna uthenga odandaulayo ndi wina wapadera okhuzidwa za zikalata zodandaula zomwe zaperekedwa kwa mkulu wa bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga pasanathe masiku asanu ogwira ntchito kuchokera tsiku lolandira pemphoro kuti bungwelo lidziunike malingana ndi gawo laling'ono (1) la malamulo

24.__(1) Bungwe kapena nthambi ya boma idzakhazikitsa ndondomeko zounika madandaulo okhudza mapempho authenga kuchokera kwa anthu odandaula.

(2) Odandaula sadzalipitsidwa ndalama chifukwa chopempha kuti bungwe liunikenso chiganizo chake chokhuza pempho lopeza uthenga.

(3) Wamkulu wa bungwe lomwe kukupezeka uthenga adzasankha m'dindo wamkulu ochokera ku bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga yemwe sanatenge nawo gawo poyendetsa pempho loyambirira, kuti adziunike momwe anachitira:

Adindo okwana atatu atha kusankhidwa kuti aunike momwe ndondomeko inayendera

(4) Odandaula ndi m'dindo opereka uthenga adzapatsidwa mwayi opereka mbali yawo pomwe ndondomeko younika ikuchitika.

(5) Zotsatira za kuunika zizaperekedwa kwa mkulu wa bungwelo kuti avomereze ndipo kenaka wamkulu wa bungwelo azadziwitsa odandaula powalembera chikalata za chiganizo chomwe chakonzedwa ataunikanso.

(6) Ndondomeko younikanso siyizatenga masiku odutsa makumi awiri ndi limodzi kuchokera tsiku limene ofuna uthenga anapereka pempho lake kuti liunikidwe.

GAWO 6_KUUNIKIDWA KWA CHIGANIZO CHA NTHAMBI YA BOMA NDI BUNGWE LA MALAWI HUMAN RIGHTS COMMISSION

25. Munthu odandaula akagwiritsa ntchito njira zonse zofuna kuti pempho lake liunikiridwe ndi nthambi ya boma komwe kukupezeka uthenga, atha kusuma ku bungwe la Malawi Human Rights Commission pogwiritsa ntchito fomu 6 yomwe ili mu ndondomeko yachiwiri ya lamulo, kuti chiganizo cha mkulu wa nthambi ya boma lomwe kukupezeka uthenga chiunikidwenso.

26. Odandaula komanso bungwe kapena nthambi ya boma yomwe kukupezeka uthenga adzapatsidwa mwayi onena mbali yawo nthawi yomwe kuunikiranso kukuchitika.

27.__(1) Popanga chigamulo monga zalembedwera pa gawo 44(6) ya Malamulowa, Bungwe la Malawi Human Rights Commission lidzagwiritsa ntchito zomwe lapeza kudzera_

(a) Kufunsa;

(b) Kufufuza;

(c) Kuunika zomwe zasungidwa kapena kulembedwa zokhudza pempolo:ndi

(d) Zomwe okhudzidwa ndi osumilidwa apereka ndi kunena

(2) Pasanathe masiku asanu ndi awiri chipangireni chiganizo, a Malawi Human Rights Commission azadziwitsa polembera odandaula ndi bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga za chiganizo chawo.

(3) Bungwe la Malawi Human Rights Commission lidzapereka fotokope ya chigamulocho kwa__

(a) odandaula;

Ndondomeko ya kuwunika kwa mkati

Kuunikidwa kwa chiganizo ndi Malawi Human Rights Commission

Ufulu omvedwa

Chigamulo

(b) Kwa ena apadera omwe akhudzidwe ndi chigamulocho; ndi:

(c) Bungwe kapena nthambi ya boma komwe kukupezeka uthenga.

(4) Ngati bungwe la Malawi Human Rights Commission lipanga chiganizo chakuti munthu odandaulayo akuyenera kupatsidwa mwayi opeza uthenga omwe anapempha, chigamulocho chidzaika m'ndandanda wazoyenera kuchita pokwaniritsa zomwe zagamulidwa m'nthawi yoikika.

(5) Bungwe kapena nthambi ya boma komwe kukupezeka uthenga lidzaika chiganizochi mu gawo laling'ono (4) m'nthawi yomwe yaikikayo, ndipo mkulu wa bungwe lomwe kukupezeka uthenga adzapereka lipoti lakuti wakwaniritsa zomwe zinagamulidwa ku Malawi Human Rights Commision.

(6) Pasanathe masiku makumi atatu chilandilireni lipoti monga mwa lamulo laling'ono la gawo (5), Bungwe la Malawi Human Rights Commision lizadziwitsa munthu odandaula ndondomeko zomwe bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga latsata potsatira chigamulo cha Bungwe la Malawi Human Rights Commission.

GAWO 7__ZINA ZOONJEZERA

Kukaniza kupereka uthenga

28.__(1) Md'indo opereka uthenga azaganiziridwa kuti walepheretsa kupereka uthenga ngati__

(a) uthenga sunaperekedwe ngakhale ofuna uthenga wakwaniritsa zoyenera zonse kuti uthenga uperekedwe malingana ndi gawo 5 la Lamulo;

(b) uthenga sunaperekedwe m'nthawi yoikika popanda chifukwa chomveka: ndi

(c) uthenga sunaperekedwe kudzera mu ndondomeko yomwe anagwirizana popanda chifukwa chomveka.

(2) Bungwe la boma lomwe kukupezeka uthenga lizakhazikitsa ndondomeko zoletsa kukaniza kupereka uthenga pa zifukwa zosakwanira.

Ndalama zogwiritsira ntchito

29. Munthu yemwe wagwiritsa ntchito uthenga m'njira yosiyana ndi imene uthengawo unapemphedwera ndipo kugwiritsa ntchito koteroko ndikonyazitsa osunga uthenga kapena ena okhudzidwa, munthuyo adzakhala kuti waputa mlandu omwe angalangidwe nawo malingana ndi gawo 54 la Lamulo.

Ndondomeko za kagwiridwe ka ntchito

30. Nthambi iliyonse ya boma idzaika padera ndalama za mu ndondomeko ya chuma cha boma yapachaka zogwiritsa ntchhito kupititsa patsogolo kuthekera kopeza uthenga.

31. A Nduna atha kudzapereka ndondomeko zakagwiridwe ka ntchito momwe angachitire kuti akwaniritse Malamulowa.

NDONDOMEKO YOYAMBA (regs. 9 and 10)

MITENGO

Mitengo yotsatilayi izagwiritsidwa ntchito pa ndondomeko yopempha uthenga-



| | *Chinthu* | *K t* |
|---|---|---|
| (1) | Kupanga fotokope mfundo zolondolera za Malawi Human Rights Commission | 10,000. 00 |
| (2) | Kupanga fotokope Buku La Uthenga. | 10,000. 00 |
| (3) | Mitengo yoikika | |
| (4) | Mitengo yodutsa yoikika yomwe yalembedwa mu gawo 3 | 5,000. 00 |
| (*a*) | Kupanga fotokope, pa tsamba . . . . | 30. 00 |
| (*b*) | uthenga onse kapena gawo ukalembedwa_ | |
| | (i) mu njira ina, yolipira isapitilire | 50. 00 |
| | (ii) pa tsamba la braille . . . . | 00. 00 |
| | (iii) pa tsamba la malembo aakulu. | 100. 00 |
| | (iv) pa CD . . . . . . . . | 1,000. 00 |

NDONDOMEKO YACHIWIRI (reg. 11)

FOMU 1

PEMPHO LOFUNA KUPEZA UTHENGA

GAWO A_TSATANE LA OSUNGA UTHENGA

Dzina la bungwe/nthambi ya boma lomwe kukupezeka uthenga...............................................

Keyala ya bungwe/ osunga uthenga...........................................................................

Dera (Boma/Tauni/Mzinda/TA/Mudzi)..............................................................

GAWO B_TSATANE WA OFUNA UTHENGA

Dzina Lonse:...........................................................................................

Tsiku Lobadwa...........................................................Mamuna/Mkazi....................

Nambala ya Chiphaso Chaunzika................................................................

Keyala.....................................................................................................

Dera lomwe amakhala......................................................................

Nambala ya Foni.......................................................................................

Keyala ya Imelo……………………………….................……………………………….……..

## GAWO C_TSATANETSATANE WA MUNTHU YEMWE AKUIMILIRIDWA PA PEMPHO

(Zizalembedwa ngati pempho likuchitika m'malo mwa munthu wina)

Tsatanetsatane wa munthu yemwe pempho likuchitika m'malo mwake (Chonde phatikizani zikalata zomwe zikutsimikizira kuti ndinu oloredwa kuti muimire munthu winayo)

Dzina: ………………………...................................……………………………………………

Keyala: ………………………...............................................…………………………………....

........................................................................................................................................

Nambala ya Chiphaso: ……………….......................................………………………………....

## GAWO D_TSATANETSATANE WA UTHENGA OMWE UKUFUNIDWA

Perekani tsatanetsatane wa mtundu wa uthenga omwe mukufuna ndi zifukwa zake.

Muphatikizenso zinthu zomwe zingathandize kuti uthengawo upezeke monga kochokera, olemba, tsiku losindikiza, ndi zina

…..………………………………………………………………………………………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

Fotokozani chifukwa chomwe mukufunira uthengawu ndi kufunika kwakuti uthengawu uperekedwe kwa inu.

…..………………………………………………………………………………………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

…..………………………………………………………………………………………………

……………………………………………………………………………..…………………

……………………………………………………………………………..…………………

## GAWO E_KALEMBEDWE KA UTHENGA OMWE WAPEMPHEDWA

Nenani kalembedwe ka uthenga komwe mukufuna, mwachitsanzo osindikiza, kapena kudzera pa kompyuta ndi zina zotero

1. Kusindikiza monga mwa nthawi zonse ( )
2. Kusindikiza kwa Braille ( )
3. Njira ina (tchulani mtundu wina wakasindikizidwe)...............………………………..

Zasayinidwa pa …………………...........……tsiku la… mwezi wa........... 20 …....................

……………………………………………………………
*Sayini ya ofuna uthenga*

FOMU 2 (regs. 13)

YANKHO LA PEMPHO LOFUNA KUPATSIDWA MWAYI OPEZA UTHENGA/KUPATSIDWA GAWO CHABE/KUKANIZIDWA

TSATANETSATANE WA BUNGWE/NTHAMBI KOMWE KULI UTHENGA

Dzina la Bungwe/kopezeka uthenga:...……………………………........…………………….........

Keyala:...........................................................................................................................................

Nambala ya Foni:…………………........………………………………………………………….

Imelo:………………………...............…………………………………………………………......

Tsiku:…………………………………....………………………………………………………..

TSATANETSATANE WA OFUNA UTHENGA

Dzina Lonse.……………………....…………………………………………………………….…

Tsiku Lobadwa…………………………….............................Mamuna/Mkazi…......……....

Nambala ya Chiphaso chaunzika……..................……………………………………………......

Keyala…..……..................………………………………………………….....................................

Dera lokhala…………………………....…………………………………….……………........

Nambala ya Foni…………………………...............……………………………………………......

Imelo………………………………......................……………………………………..................

YANKHO

Potengera pempho lanu lofuna uthenga okhuza ………………………………………..........................
Lomwe linaperekedwa pa ..................................................Pempho lanu laperekedwa/laperekedwa kwa gawo chabe/lakanidwa.

ZIFUKWA

……………………...............................................................……………………………………..

…………………............................................................................................……………..........

.........................................................................................................................................................

.........................................................................................................................................................

Zikalata zophatikizidwa…………………………....………………………………..................................

Dzina la m’dindo opereka Uthenga:……….................………………………………………..

SAINI:………….............................…………………………………………………….........

Chidindo:

Uthenga walandiridwa ndi:……………………………………………………………………….

Saini:……………………………………......… Tsiku:……..........……..……….

FOMU YACHITATU (reg. 15)

KUPEREKA UTHENGA KWA ENA OKHUDZIDWA

GAWO A

Tsatanatsatane wa ena okhudzidwa (Dzina ndi Keyala)

………………………………………………………………………..……………

..………………………………………………………………………………………

Talandira pempho lofuna kupeza uthenga kuchokera kwa munthu yemwe tsatanetsatane wake walembedwa m'musimu Munthuyu wapempha uthenga uwu

……………………………………………………………………..………………

.....…………………………………………………………………………………

Gawo 20 la Lamulo lopereka kuthekera kopeza uthenga likunena kuti ngati uthenga omwe wapemphedwawo ungakhale wachinsinsi kapena ngati ungakhudze anthu ena, anthu enawo akuyenera kudziwitsidwa za pempholo. Pachifukwa ichi mukupemphedwa pasanathe masiku khumi ogwira ntchito kuchokera tsiku lachidziwitso, kunena ngati pali kutsutsa kuti uthenga opemphedwawo uperekedwe ndipo chonde mupereke zifukwa.

M'munsimu muli zambiri zokhudza munthu yemwe wapempha uthenga.

Dzina Lonse.……………………...……………………………………………….…

Tsiku Lobadwa……………………………...................................Mamuna/Mkazi......……..

Nambala ya Chiphatso chaunzika………..................………………………………………

Keyala...........................................................................................................................

Dera lokhala…………………………....……………………………………..………………

Nambala ya Foni…………………………...............……………………………………….

Imelo…………………………………....................…………………………….…

Dziwani kuti mukalephera kuyankhapo pa chidziwitsochi mu nthawi yoikika, zotsatira zake zidzakhala kupereka uthenga omwe unapemphedwawo kwa opempha uthenga.

Dzina: ………………………………..………………… Saini:……......……………......

*M'DINDO OPEREKA UTHENGA*

Tsiku: ……………………………………………

FOMU 4 (reg. 20)

KUPITITSA PEMPHO LOFUNA UTHENGA KU BUNGWE LINA LA BOMA KOMWE KUKUPEZEKA UTHENGA

GAWO A_TSATANE WA BUNGWE LA BOMA KOMWE KUKUPEZEKA UTHENGA

Dzina la Bungwe/Kopezeka uthenga..…………………………………………………………...........

Keyala ya Bungwe/osunga uthenga………………………………......……………………...........

Dera(Boma/Tauni/Mzinda/TA/Mudzi………...............……………………………………….........

GAWO B TSATANE WA OFUNA UTHENGA

Dzina Lonse.……………………....……………………………………………………………..…

Tsiku lobadwa……………………………….……………..............…Mamuna/Mkazi………..…....

Nambala ya Chiphaso chaunzika……………..........…………………………………………….....

Keyala….…....................…………………………………………….........................................

Dera lokhala……………………………………………........………………….……………….......

Nambala ya Foni…………………………….....................…………………………………….....

Imelo……………………………….....................………………………………………...............

GAWO E

Potsatira pempho lofuna kupeza uthenga lomwe munapereka pa................ tati tikutumizeni kwa ............................................................................................................ omwe akupatseni uthenga wa................……………………………………………………………………

……………................................................ : ……………………………………………

*Sayini* *Dzina*

…………………………………………………………………………

*Sayini*
*M'DINDO OPEREKA UTHENGA*

Tsiku: ……………………………………………

FOMU 5 (reg. 23)

PEMPHO LAKUTI BUNGWE LIUNIKE CHIGANIZO CHAKE

GAWO A_TSATANE WA BUNGWE/NTHAMBI KOMWE KUKUPEZEKA UTHENGA YOMWE CHIGANIZO CHAKE CHIUNIKIDWE MU PEMPHOLI

Dzina la Bungwe/Osunga uthenga…………………...........…………………………..

Keyala ya Bungwe/komwe kukupezeka uthenga……..……..………………………………

Dera (Boma/Tauni/Mzinda/)……………...............……………………..………………

Imelo……………………....................……………………………………………

Nambala ya Foni……………..................………………………………………………

GAWO B_TSATANE WA OFUNA UTHENGA

Dzina Lonse.……………………....……………………………………………………..…

Tsiku Lobadwa…………..……………………..................................Mamuna/Mkazi....……......

Nambala ya Chiphaso chaunzika……..................…………………………………….....

Keyala.................................................................................................................................

Dera lokhala……………………....……………………………………..……………........

Nambala ya Foni…………………………..............………………………………………......

Imelo……………………………….....................……………………………….................

GAWO C_TSATANE WA MUNTHU YEMWE UTHENGA UKUPEMPHEDWA M'MALO MWAKE

Lembani ngati pempho laperekedwa m'malo mwa munthu wina)

(Tsatane wa munthu yemwe uthenga ukupemphedwa m'malo mwake)

Dzina Lonse.……………………....……………………………………………………..…

Tsiku Lobadwa…………..……………………..................................Mamuna/Mkazi.......……..

Nambala ya Chiphatso chaunzika……..................……………………………………

Keyala.................................................................................................................................

Dera lokhala……………………....……………………………………..……………........

Nambala ya Foni…………………………..............………………………………………......

Imelo……………………………….....................……………………………….................

Chifukwa/zifukwa zoyimilira opempha uthenga.....………….............……………………....

……………………...........………………………………………………………………....

…………………………...……………………………………………………………………...

…………………………....…………………………………………………………………......

.................................................................................................................................

.................................................................................................................................

GAWO D_CHIDULE CHA PEMPHO

(Perekani chindunji cha pempho lanu loti mupeze uthenga ndiponso perekani chifukwa choti mupatsidwe uthengawo. Perekani zifukwa zomwe zapangitsa kuti musagwirizane ndi chiganizo cha m'dindo opereka uthenga)

…………………………………………………………………………………..…………

…………………………………………………………………………………..………………

…………………………………………………………………………………..………………

…………………………………………………………………………………..………………

GAWO E_MTUNDU WA CHITHANDIZO CHOPEMPHEDWA

(Fotokozani mtundu wa chithandizo chomwe mukufuna kuchokera kwa Mkulu wa Bungwe lomwe pempho lofuna kupeza uthenga linaperekedwa)

……………………………………………………………..……………………………..

……………………………………………………………..……………………………..

……………………………………………………………..……………………………..

……………………………………………………………..…………………………......

Zasainidwa ku ……………………………pa…. tsiku ndi mwezi wa …………20 …..............

……………………………………………………………

*Saini ya ofuna uthenga*

Muphatikize mafotokope a zikalata zotsatilazi ngati zilipo

1. Fomu yopemphera uthenga
2. Yankho la pempho lopeza uthenga la m'dindo opereka uthenga

FOMU 6 (reg. 25)

PEMPHO LOTI CHIGANIZO CHA BUNGWE LA BOMA LOMWE KUKUPEZEKA UTHENGA CHIUNIKIDWE NDI ENA

GAWO A_TSATANE WA BUNGWE LOMWE CHIGANIZO CHAKE CHIKUYENERA KUUNIKIDWA

Dzina la Bungwe……………………........…………………………………………….............

Keyala ya Bungwe………………………………..……………..……………………..............

Dera (Boma/Tauni/Mzinda/TA/Mudzi………..…………………………………………..........

Imelo…………………….………………………………………………………...................

Nambala ya Foni.....……………………......………………………………..………….....

GAWO B_TSATANE WA ODANDAULA

Dzina Lonse.……………………....………………………………………………………..…

Tsiku lobadwa…………………………….................................Mamuna/Mkazi.....……......

Nambala ya Chiphatso Chaunzika………...............………………………………

Keyala.........................................................................................................................

Dera lokhala……………………....……………………………….……………….......

Nambala ya Foni………………………............……………………………………......

Imelo………………………………................…………………………………...............

GAWO C TSATANE WA MUNTHU YEMWE PEMPHO LIKUPEREKEDWA M'MALO MWAKE

Lembani ngati pempho likuperekedwa m'malo mwa munthu wina)

Dzina lonse....…………………....…………………………………………………..…

Tsiku lobadwa.......…………………………..............................Mamuna/Mkazi..……......

Nambala ya Chiphatso Chaunzika.……...............………………………………...

Keyala.........................................................................................................................

Dera lokhala………………………....……………………………….……………......

Nambala ya Foni..………………………............…………………………………….....

Imelo……………………………….................…………………………………...............

Wopempha uthenga ndi:

……………………………………………………………………………………..…

……………………………………………………………………………..………

GAWO D_KUKWANIRITSA NJIRA ZONSE ZOUNIKIRA CHIDANDAULO

(Chonde lembani ndondomeko zomwe munatsata pogamula nkhani ndi bungwe la boma losunga uthenga komanso chiganizo chomwe bungwelo linapanga pamapeto a zonse)

……………………………………………………………………...……………………

……………………………………………………………………..……………………

………………………………………………………………………..…………………

GAWO E__MTUNDU WA DANDAULO (CHONDE ZUNGULIZANI KAPENA CHONGANI POYENERERA)

Dandaulo likukhudza_

1. Kukanizidwa mwayi opeza uthenga kuchokera kwa osunga uthenga.
2. Kuchuluka kwa ndalama zoyenera kulipira.
3. Kukanika kwa osunga uthenga kuchita zinthu mu nthawi yoikika
4. Dandaulo lina liri lonse lokhudza pempho lofuna kupeza uthenga (Chonde tchulani)

…………………………………………………………………..…………………………

…………………………………………………………………..………………………

…………………………………………………….....................…………………

GAWO F_ CHIDULE CHA PEMPHO

Perekani chidule cha dandaulo lanu komanso mulongosole zomwe zinachitika kapena chomwe chakupangitsani kuti mudandaule. Chonde ngati zili zotheka mutchule dzina la fayilo kapena chikalata ndi masiku okhudzana ndi dandaulo komanso tsiku lomwe uthenga unapemphedwa ndi tsiku lomwe yankho linalandiridwa)

………………………………………………………………..……………………………

…………………………………………………………………..…………………………

…………………………………………………………………..…………………………

GAWO G_MTUNDU WA CHITHANDIZO CHOPEMPHEDWA

(Longosolani mtundu wa chithandizo chomwe mukufuna kuchokera ku Malawi Human Rights Commission)

……………………………………………………………………………………….…

……………………………………………………………………………………..………

……………………………………………………………………………..………………

…………………………………………………………………………………..…………

Zasayinidwa pa………………………tsiku…..........mwezi……………chaka …….................

…………………………………………………………….

*Sayini ya odandaula*

Lapangidwa pa 13th January chaka cha 2021.

G. KAZAKO
*Nduna Yofalitsa Nkhani*

(FILE NO. IFN/ADMIN/01/04)

Zasindikizidwa ndi MAKINA OSINDIKIZIRA A BOMA, Lilongwe, Malawi_6697__(*Mtengo K2,000.00)*